EXAMINATIONS No:________________________

# ZOMBA URBAN DISTRICT ASSESSMENT

## 2025 PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE EXAMINATION

# CHICHEWA

## (100 MARKS)

TSIKU :30th January, 2025. Subject Number:P033

Nthawi : 2 ¼ HRS

From: 12:00 – 2:15 PM

DZINA LANU____________________________________________________________
(yambani ndi la bambo)
DZINA LA SUKULU YANU:____________________________________________________

| Funso | Chongani zomwe mwayankha | Muno musalembemo | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| 5 | | | |
| 6- 10 | | | |
| 11-15 | | | |
| 16-20 | | | |
| 21-25 | | | |
| 26-30 | | | |
| 31-35 | | | |
| 36-40 | | | |
| 41-45 | | | |
| | | | |

MALANGIZO

1. Onetsetsani kuti pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa asanu ndi limodzi.
2. Pepala ili lili ndi magawo anayi **A,B,C** ndi **D**.
3. Lembani **dzina lanu** ndi **dzina la sukulu yanu** pamwamba pa tsamba lililonse.
4. Lembani **nambala ya mayeso** pamwamba pa tsamba lililonse.
5. Lembani **chimangirizo** kapena **kalata** mu Gawo **A** ndipo muyankhe mafunso onse mu Gawo **B,C** ndi **D**.
6. Yankhani mafunso a mugawo **B** ndi **C** m'mipata yomwe yaperekedwa pansi pa funso lilonse..
7. Yankhani mafunso amu gawo **D** pozunguliza limbo lokhoza pafunso lililonse..
8. Perekani pepala lanu kwa woyang'anira mayeso pamene mwauzidwa kuti mutero.
9. Mu tebulo lomwe mwapatsidwali, chongani mafunso omwe mwayankha kupatula mafunso 6 mpaka 45.

GAWO A (MALIKISI 30)

Langizo

Yankhani funso limodzi lokha mwa mafunso awiri ali m'munsiwa. Sankhani chimangirizo kapena kalata. Mawu a chimangirizo kapena kalata yanu asachepere 100 koma asabzole 150.

1. Lembani chimangirizo pa mutu uwu "BOMA LAKWATHU" Mwazina tsatani izi polemba:

Ndime yoyamba

- Tchulani dzina la boma la kwanu.
- Chigawo chomwe bamali likupezeka.
- Bomali lidachita malire ndi maboma ati?

Ndime yachiwiri

- Fotokozani mitundu ya anthu a m'bomali.
- Fotokozani magule amene anthu a m'bomali amakonda kuvina.
- Longosolani momwe anthu a m'bomali amapezera chuma.

Ndime yachitatu

- Fotokozani mavuto omwe anthu a m'bomali amakumana nawo.
- Njira zomwe mavutowo angathetsedwere.

KAPENA

2. Lembani kalata kwa agogo anu yowauza kuti mudzapita kukawachedzera mukalemba mayeso anu a sitandade 8.

Mwa zina tsatani izi polemba kalata yau

Ndime yoyamba

- Cholinga cha kalata yanu
- Tsiku lomwe mudzapite kwa agogo anuko
- Nthawi yomwe mudzakhale muli ku kutchuthiko

Ndime yachiwiri

- Yemwe mudzapite naye kutchuthiko
- Zomwe mudzatenge popita kutchuthiko
- Chisangalalo chomwe mudzakhale nacho mukazapita kutchuthiko

Nime yachitatu

- Zomwe mukuyembekezera kudzachita kutchuthiko.

GAWO B (MALIKISI 20)

KUMVETSA NKHANI

3. Werengani nkhani yomwe ili m'musimu mosamala kenako muyankhe mafunso otsatirawo

Mudzi utatha kumanda, m'dzukulu m'modzi adapita kukauza a mfumu Kalenga kuti mwambo wamaliro uyambe. Amfumu atawona kutha kwa mudziwo, mosakhalitsa adzukulu adatulukira atandondozana ngati midzodzo chithatha chili m'manja. Apa nkuti wotsogolera mwambo atauzanso anamalira ndi anthu onse zoyamba mwambowu. Atatero anthu angapo adatulutsa mfumu kukonzekera kupita kunsamba mfumu.

Wotsogolera mwambo adaimirira nayamba kuyankhula motere: “ Pepani anamalira nonse, pepani gogo chalo Kawinga, pepani mfumu Kalenga ndi mfumu zonse, pepani mayi ndi abambo, anyamata ndi atsikana. Tsopano tikufuna tiyambe mwambo wa maliro. Chonde tiyenitikhale chete kuti tipereke ulemu woyenera pamaliro pano komanso kuti timvane. Tidziwa maliro alibe chidzolowezi nanga tingatani poti ndi mmene kunalembedwera, motero pepani tiyeni tiugwire mtima. Panthawi ino tipemphe akuchikazi kuti atiyankhule.

“ulemu waperekedwa kale. Tithokoze nonse amene mwazatikuta tikuthokozeni chifukwa mwasiya ntchito zanu kuzakhala nafe panthawi yowawitsayi. Inutu mwachita izi poti maliro nkulirana. Tsopano ndifotokoze za matenda omwe mfumu yathuyi imadwala. Malemuwa adangogwa pomwe amati alowe mnyumba mwawo dzulo. Mosazengereza tidapita nawo ku chipatala cha Ntaja komwe atawapima adawapeza ndi malungo aakulu. Ali mkati molandira mankhwala tidangoona akutigwira mosakhalitsa kupita kudali komweko. Dandaulo lathu ndi ana, adzukulu ndi mferekazi omwe malemuwa asiya. Zateromu mtengo wakachere wagwa. Anzathu akuchimuna tiyeni tigwirane manja posamalira anthuwa poti mwana wanzako ndi wako yemwe ukachenjera manja umadya naye.

Tchulani dzina la chipatala komwe wotisiyayu adatengedwera.

_______________________________________________(Maliksi 1)

a. Ndani anapita kukauza a mfumu kuti mudzi watha kumanda?

_______________________________________________(Malikisi 1)

b. Pezani mawu mnkhaniyi omwe akufana matanthauzo ndi awa:

(i). Manda _______________________________________( Malikisi 1)

(ii). Namfedwa ____________________________________(Malikisi 1)

(iii). Kutsanzika ___________________________________(Malikisi 1)

c. Kodi maliro adachitika m’mudzi uti?

_______________________________________________(Malikisi 1)

d. Perekani matanthauzo a mikuluwiko iyi

(i). Mtengo wakachere wagwa ______________________________

_______________________________________________(Malikisi 2)

(ii). Tiugwire mtima______________________________________

_______________________________________________(Malikisi 2)

(iii). Tigwirane manja ____________________________________

_______________________________________________(Malikisi 2)

e. Ndi dandaulo lanji lomwe woyimira anamalira adapereka chifukwa cha imfa ya malemuwo?

_______________________________________________________

_______________________________________________(Maliksi 2)

f. Kodi womwalirayu amadwala chiyani?

_______________________________________________________

____________________________________________(Malikisi 1)

g. Kodi woyendetsa mwambo amatanthauzanji ponena kuti tithokoze nonse mwazatikuta

______________________________________________________________

____________________________________________(Malikisi 2)

h. Perekani mutu wa nkhaniyi

______________________________________________________________

____________________________________________(Malikiisi 2)

GAWO C (MALIKISI 10)

4. Werengani kankhanika ndipo muyankhe mafunso otsatirawa

Nkhani yomwe tabwerera pano ndi yakuti akudandaula ndi makhalidwe oipa a ana athu. Anawa sakusamala katundu wa sukulu ndipo adaphwanyanso magalasi m’mazenera.

Tsopano yankhani mafunso awa:

a. Kodi ndi malonje anji mwawerengawa?

__________________________________________________(Maliksi 1)

b. Kodi malonjewa kuchitika kuti?

__________________________________________________(Malikisi 1)

c. Ndani yemwe angayankhule malonjewa?

__________________________________________________(Malikisi 1)

d. Kodi ndalama zimene zimaperekedwa kwa sing’anga asanapite kofuna mankhwala zimatchedwa chiyani?

______________________________________________________________

____________________________________________(Malikisi 1)

e. Kodi woguza njinga ayenera kuyenda mbali iti pamsewu.

__________________________________________________(Maliksi 1)

5. Kupanga ziganizo

Lembani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa.

a. Bzala ____________________________________________(Malikisi 1)

b. Mtudzu __________________________________________(Malikisi 1)

c. Monyang’ama________________________________________(malikisi 1)

d. Mfumakazi________________________________________(Malikisi 1)

e. Ndwi ____________________________________________(Malikisi 1)

GAWO D. (MALIKISI 40)

Zunguzlizani lembo lokhoza (A,B,C kapena D) Mafunso otsatirawa.

**Mafunso 6 mpaka 10: sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.**

6. Ndine mwana wa a kachere.

   A. Mlowammalo
   C. Mfotokozi

   B. Mneni D. Mperekezi

7. Khasu la a Phiri lasowa

   A. Mlumikizi C. Mvekero

   B. Mneni D. Mperekezi

8. Mwana wanga wagwera pachitsime.

   A. Muonjezi C. Mfotokozi

   B. Dzina D. Mneni

9. Chisomo adakomoka chifukwa cha mantha.

   A. Muonjezi C. Dzina

   B. Mneni D. Mfotokozi

10. M'mera uli biriwiri m'munda

    A. Mfuwu C. Mneni

    B. Mvekero D. Mfotokozi

**Mafunso 11 mpaka 15 sankhani chiganizo chomwe chili ndi zizindikiro zamkalembedwe zoyenera.**

11. A. Uziyenda mofulumira tadala.

    B. Uziyenda, mofulumira Tadala.

    C. Uziyenda mofulumira, Tadala.

    D. "Uziyenda mofulumira", Tadala

12. A. Kodi uli ndi ana angati? Eliza.

    B. Kodi uli ndi ana angati Eliza?

    C. "Kodi uli ndi ana angati Eliza?"

    D. Kodi uli ndi ana angati, Eliza?

13. A. Mayo! njoka yandiluma.

    B. Mayo, njoka yandiluma.

    C. Mayo! Njoka yandiluma.

    Mayo njoka yandiluma!

14. A. Chikumbutso adati, "Ndalephera mayeso."

    B. "Chikumbutso adati," ndalephera mayeso.

    C. Chikumbutso adati, "ndalephera mayesio."

    D. Chikumbutso adati ndalephera mayeso.

15. A. Maria, namwino wapiti kuchipatala.

    B. Maria, namwino wapiti kuchipatara.

    C. Naria namwino wapiti kuchipatala.

    D. "Maria namwino wapiti kuchipatala.

**Mafunso 16 mpaka 20 sankhani magulu a mayi na omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo.**

16. Agogo agula nsomba zabwino

    A. Mu - , Mi- C. U-, Ma-

    B. Li--, Ma- D. I - , Zi-

17. Kalulu ndi nyama yochenjera.

    A. Mu-, A- D. I-, Zi-

    B. Ka-, Ti- C Chi-, Zi-

18. Dzino langa likupweteka.

    A. I-, Zi C. Li-, Ma-

    B. M-, Mi D. U-, Ma-

19. Kulima nkopindulitsa

    A. Ku-, Pa-, Mu- C. I-, Zi-,

    B. Ku + Tsinde la mneni D. Li-, Ma-

20. Mkodzo wa mphaka umanunkha kwambiri.

A. U-, Ma- C. Ku-, Pa-, MU-

B. Li-, Ma- D. Mu-, Mi-

**Mafunso 21 mpaka 23: sankhani matanthauzo a ndagi/ zilapi zotsatirazi.**

21. Khasu la aPhiri kwina kolimira kwina kosalazira

A. Mthiko C. Phazi

B. Chipande D. Dzira

22. Akanditema bala silioneka.

A. Chithunzithunzi C. Madzi

B. Mchenga D. Dzita

23. Agogop akwathu timawatembenuza pachaka kamodzi.

A. Mthumba C. Mapepara

B. Mzere D. Sukulu

**Mafunso 24 mpaka 27 sankhani mitundu ya nthambi za ziganizo zomwe zatsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.**

24. Sindikudziwa chimene akudwala,

A. Ya mfotokozi C. Ya muonjezi

B. Ya dzina D. Yoima payokha

25. Aphunzitsi athu agona msanga poti atopa kwambiri.

A. Ya mfotokozi C. Ya dzina

B. Yoima payokha D. Yoima payokha

26. Kachipande wadya mbatata yomwe ndidagula dzulo.

A. Ya dzina C. Ya mfotokozi

B. Ya Muonjezi D. Yoima payokha

27. Iwo andiona pomwe ndimatuluka mnyumba.

A. Ya muonjezi C. Ya mfotokozi

B. Yoima pa payokha D. Ya dzina

**Mafunso 28 mpaka 30: sankhani ntchito za "ndi" mziganizo zotsatirazi**

28. Ndi ufulu wanga kulemba mayeso

A. Mlowammalo C. Mvekero

B. Mperekezi D. Mneni

29. Iwo amakhala pafupi ndi ife.

A. Mperekezi C. Mlumikizi

B. Mneni D. Mlowammalo.

30. Ndidya mitanda itatu basi.

A. Mneni C. Mlowammalo

B. Mvekero D. Mperekezi

**Mafunso 31 mpaka 33 : sankhani mikuluwiko yofanana m'matanthauzo ndi yotsatirayi.**

31. Nsabwe yoyendayenda idakumana ndi chala.

A. Mwana wa mwini ndi gaga sawundika

B. Mwana wang'ono sakulira dziwe limodzi

C. Pamodzi modzi padaoletsa dzungu

D. Mwala wogubuduka suyanga ndere

32. Wokaona Nyanja adakaona ndi mvuwu zomwe

A. Ukayendera mzengo usati asakhwi afumbula

B. Ukayenda mtchire wayendera zonse

C. Zengerezu adalinda kwawukwawu

D. Mawu akulu akoma akoma akagonera

33. Timba sachepa ndi madzira ake.

A. Mako ndi mako usamuone kuchepa mwendo.

B. Nyumba yamwini saotchera mbewa

C. Chimanga chilora wopanda mwana

D. Mwini phale sakuda chala.

**Mafunso 34 mpaka 36: sankhani nthawi za aneni omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo.**

34. M'busayo azizapempheretsa ku Salima.
    A. Yatsopano yopitirira
    B. Ya mtsogolo
    C. Yamstogolo yopitirira
    D. Ya tsopano yakawirikawiri

35. Alinafe ankagulitsa nyumba kumagomero.
    A. Yamtsogolo yopitirira   C. Yakale
    B. Yatsopano yopitirira   D. Yakale yopitirira

36. Asiyatu wadya msima
    A. Yatsopano   C. Yakale
    B. Yatsopao yathayi   D. Yatsopano yopitirira

**Mafunso 37 mpaka 40: sankhani ntchito za mayina mziganizo zotsatirazi**

37. Galu akuthamangitsidwa ndi fisi
    A. Kukhala pamthera mkhani
    B. Kukhala mwini nkhani
    C. Kukhala dzina loyitanira
    D. Kukhala dzina lapadera

38. Chikapa, mlembi sabwera lero.
    A. Kukhala dzina loyitanira
    B. Kukhala panthera nkhani
    C. Kukhala mwini nkhani
    D. Kukhala dzina lapadera

39. Pita ukandigulire mango, Chifuniro.
    A. Kukhala mwini nkhani
    B. Kukhala dzina lapadera
    C. Kukhala dzina loyitanira
    D. Kukhala panthera nkhani

40. Mayeso akulembedwa ndi Vanessa.
    A. Kukhala mwini nkhani
    B. Kukhala dzina lapadera
    C. Kukhala panthera nkhani
    D. Kukhala dzina loyitanira

MAFUNSO ATHERA PANO